

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

MPHAMVU YA MATAMANDO

Yehosafati, mfumu ya Ayuda, anaweramira pansi pamaso pa Mulungu mu kupemphera ndi kusala kudya. Monga akunenera pa 2 Mbiri 20, khwimbi lalikulu la adani a Ayuda, linasonkhana kuti lilimbane ndi Yehosafati pankhondo. Poopa, makamaka pozindikira kuti anthu ake paokha analibe mphamvu zolimbana ndi mdani amene anali kubwerayo, iye anafuulira wa Mulungu nati, "Yehova Mulungu wa makolo athu, Inu sindinu Mulungu wa m'Mwamba kodi? Sindinu woweruza maufumu onse a amitundu kodi? Ndi m'dzanja mwanu muli mphamvu yolimba; palibe wina wakulimbana ndi Inu....Pakuti mwa ife mulibe mphamvu yakulimbana nao auniyinj ambiri awa akutidzera; ndipo sitidziwa ngati tidzatani, koma maso athu ali kwa Inu." Ndipo Yehova anayankha nati: "Musaope musatenge nkhawa chifukwa cha auniyinj ambiri awa; pakuti nkhoodoyi si yanu, koma ya Mulungu... Si kwanu kuchita nkhoodo kuno ai; chilimikani, imani, nimupenye chipulumutso cha Yehova."


M'mawa winawo, mwachikhulupiriro ndi kulimbika mtima mwa mau a Mulungu, Yehosafati anasankha oyimba, amene anapita patsogolo pa asilikali a nkhoodo ndipo amatamanda kukongola kwa chiyero cha Mulungu. "Yamikani Yehova, pakuti chifundo chake chikhala chosatha." Pamene anayamba kuyimba ndi kutamanda, Yehova anawasokoneza adani aja mwakuti anayamba kuphana okhaokha. Mulungu anapereka chigonjetso chachikulu kwa anthu ake. M'malo mong'ung'udza chifukwa cha mantha ndi kukhala kakasi chifukwa cha nyengo zosautsa zimene amadutsamo, iwo anayika chikhulupiriro chawo ndi kudalira mwa Mulungu ndipo anayimba nyimbo yotamanda Yehova.

Muli mphamvu yaikulu mu matamando! Mdaniyo amagonjetsedwa pamene Mulungu akwezedwa ndi ulemu komanso malemekezo.

Nkhondo zambiri zauzimu zagonjetsedwa pamene anthu a Mulungu anakweza mitima yawo ndi milomo yawo pa kutamanda. Matamando opita kwa Mulungu kudzera mu kufuula, kupereker umboni, kapena kuyimba nyimbo amatsekula zipata zokafika pamaso penipeni pa Mulungu, popeza Mulungu amakhala m'matamando (Masalmo 22:3). Pamene Agoliyati ndiponso malinga a Yeriko ali pamaso panu, imeneyo ndiye nthawi yotamanda Mulungu ndiponso kuvomereza ukulu wake ndi mphamvu zake. Kumbukirani kuti Aisraele anazungulira mzinda wa Yeriko kwa masiku 6 osachita phokoso. Koma pa tsiku la 7 iwo anazungulira kokwanira ka 7. Panthawi ya chi 7 imenenso inali yomaliza, anthuwo anakuwa kwambiri pamene ansembe analiza malipenga, potsatira lamulo imene Yehova anawauza, popeza Iyeyo anali atawapatsa mzindawo. Pamene anafuula, makoma a Yeriko anagwa pansi ndipo iwo analanda mzindawo (Yoswa 6:16-20). Atamandike Mulungu! Nthawi zina anthu satulutsa mau othokoza kwa Mulungu ngakhale onong'ona, ndipo iwo amadabwa kuti ndi chifukwa chiyani makoma a miyoyo yawo alipobe sakugwa. Kufuula kwenikweni kwa uzimu ndi kokhako kumene kumachokera mkati chifukwa cha Mzimu wa Mulungu. Yehova ndi wamkulu, ndipo akuyenera kutamandidwa kwakukulu.

Atamandike Yehova, ndipo kudzera mu chikhulupiriro kwa Mulungu, amene akhoza kubweretsa kusintha mu nthawi imene mdima wafika pachimake. Kutamanda kumathandiza kuti munthu alingalire pa Mulungu kusiyana ndi kukhazikika pa chifooko chake ndiponso nkhoodo zakuthupi zimene akulimbana nazo. Kutamanda kumabweza malingaliro a munthu kuti aganize za Iye amene akhoza kuchita zinthu zonse. Mu nthawi ya kukhumudwitsidwa

(Yapitirira pa tsamba 2)



"Matamando opita kwa Mulungu kudzera mu kufuula, kupereker umboni, kapena kuimba nyimbo amatsekula zipata zokafika pamaso penipeni pa Mulungu, popeza Mulungu amakhala m'matamando."

Mau a Mkonzi

Kalozera posanthula
Baibulo: Matamando

O Lemekezani Yehova

Funso Yankho

Kodi Mukudziwa?

3

4

5-6

7

8

Mau a Nyengo Yake

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

ndi kusauka m'maganizo, kutamanda Mulungu kumatsekula khomo la Kumwamba kumene mzimu umasanduka watsopano ndiponso umatsitsimutsidwa.

Mu Machitidwe 16:22-26, Paulo ndi mnzake Sila anakwapulidwa ndi zikwapu zambiri koma osalakwa ndipo kenaka miyendo yawo anayimangiriza mu matabwa. Ngati panali munthu wakuti akhoza



“Mu nthawi ya
kukhumudwitsidwa ...
kutamanda Mulungu
kumatsekula khomo la
Kumwamba kumene
mzimu umasanduka
watsopano ndiponso
umatsitsimutsidwa.”

izi za matamando ndi chigonjetso, panachitika chivomerezi chachikulu ndipo ndendeyo inayamba kugwedezeke. Makomo a ndende anatsekuka pululu ndipo maunyolo a wina aliyense anachoka. Kuwomboledwa kunafika kudzera mu njira ya kutamanda.

Mwana wa Mulungu, kweza mutu wako ndipo upereke matamando kwa Mulungu. Usakhulupirire mu zinthu zimene zili zooneka koma mwa Iye amene ali ndi mphamvu zonse kumwamba ndi panso pano. Ngakhale mdima uchuluke motani, ngakhale makoma atalike motani, ngakhale mapiri akhale aatali bwanji, ngakhale zigwa zikhale zolowa motani, ngakhale moto ukhale wootcha motani kapena mayesero achuluke motani, komabe uyang'ane kwa Yesu ndipo umutamande Iye. Umutamande Iye chifukwa cha chipulumutso. Umutamande Iye chifukwa cha chifundo chake. Umutamande Iye chifukwa cha ubwino wake ndi chikondi chake. Mphamvu ya Mulungu imagwira ntchito kudzera mu matamando ngakhale pali namondwe. Kutamanda Mulungu kumatsekula khomo lakuti Mulungu awonetsere mphamvu yake kwakukulu. Musatengere m'mene mukumvera, koma mkwezeni Ambuye ndi mtima wachiyamiko komanso matamando. Imbani ndipo fuulani popereka matamando kwa Ambuye ndipo mdaniyo adzagonjetsedwa. Tamandani Ambuye! ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvumere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Pakuti chifundo chanu chiposa moyo makomedwe ake, Milomo yanga idzakulemekezani. — Masalmo 63:3

Mutu wa ulendo uno ukukamba nkhanu ya matamando. Ngakhale kuti lili lamulo, komabe kutamanda Mulungu ndi chinthu chimene tichiyesera chamwai komanso chaulemu. Mulungu watichitira zazikulu kwambiri ifeyo, ndipo kodi tingamubwezere bwanji ndiponso kumukweza Iye ndi chipatso cha pakamwa pathu? Mitima yathu idzikhala yodzaza ndi matamando ngakhale mu nthawi zosautsa, ndipo milomo yathu ikuyenera kulemekeza Ambuye.

Pali malemba ochuluka pa mutu umenewo koposa zimene tingathe kuzikamba mu kalatayi. Chosangalatsa ndi chakuti ngakhale kuti pali zambiri zimene zaphunzitsidwa pa mutu wa kutamanda, anthu ambiri oyera mtima amaona ngati ndi chinthu chakuti munthu akhoza kuchita mwakufuna kwake, ndipo pakutero iwo amakakamira kakaka pa ziphunzitso zimene zimapezeka pa malo awiri kapena atatu basi. Palibe choonadi chimene tikuyenera kuchichepetsa, komatu tikuyenera kulabadira kwambiri za chiphunzitso chimene chimaphunzitsidwa mu Baibulo kwathunthu.

Nthawi zimene ndakhala nazo zopindulitsa pa nkhanu yokhudza kutamanda ndi pamene ndinali ine ndi Ambuye basi awiriwiri mu ofesi kapena pamene ndimayendetsa galimoto. Ngakhale zili choncho, ndimakhala wokakamizika kuletsa matamando oterewo pamene tili pagulu. Tiyeni tiime njii ndi kulimbana ndi mchenjerero a mdaniyo amene amafunitsitsa kuti aike chinthu chimene chingatiletse kuti tisalemekeze Ambuye. Kuyambira kale, oyera mtima ali ndi mbiri yabwino ya kutamanda ndi kuthokoza. Nyimbo zambiri zimene anthu a Mulungu ayimba ndi nyimbo za matamando komanso zolemekeza Ambuye. Kuli kwabwino ndi koyenera kwa Mulungu kuti atamandidwe ndi mtima umene uli wansangala komanso wofuula motsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

Pali mipingo imene poyamba inali yamphamvu ndi yodzadza ndi moyo wa mzimu wa kutamanda, koma panopa inazizira ndipo inazilala. Mulungu amafuna kuti anthu ake adzikhala oyaka moto pamene akufuna kuchita chifuniro chake. Zonedwa pakamwa pazokha ndi zosakwanira, koma makamaka moyowo umene munthu akuwukhala. Ndipo tikuwuzidwa kuti tidzikhala ndi chionetsero chakunja cha zimene zachitika mkati mwathu. Zidzakhala nthawi zimene tidzalemekeza mwachete komanso zilipo nyengo zimene padzakhala kukondwera kwakukulu. Anthu ambiri akuyamba kuperewera pa mlingo wa Baibulo pa moyo wao wa kutamanda. Kutamanda Mulungu sikuyimba mu chipembedzo m'tchalichi koma ndi moyo wa tsiku ndi tsiku woyanjana ndi Ambuye.

Kutamanda kwenikweni si kokakamidwa kapena chionetsero chochita mopereka malire, koma ndi chinthu chochitika mwaufulu kuchokera mu mtima. Ambuye akufuna kuti kudzera mwa Mzimu wake, ifeyo tichite zinthu zotheka kuti tipereke malo komanso kuthekera kwakuti matamando achitike mosavuta.

Tiyeni tifunefune Mulungu pamene tikutamanda mokhulupirika, popeza ngati Mulungu wakwezedwa, ifeyo timalemekezedwa m'mitima yathu.

Michael W. Smith

October 2019

KWEZANI MANJA OYERA

Ndidzakweza manja anga m'dzina lanu. — Masalmo 63:4

Chakhala chili chikhaliidwe cha anthu a Mulungu kuchokera ku Chipangano Chakale mpaka kufika ku Chatsopano kuti amakweza manja awo popemphera ndi kutamanda Ambuye. Pa kupemphera, zimasonyeza kudzichepetsa komanso kuonetsa kufuna pamaso pa Iye amene ali wopereka zinthu zonse. Iye amatambasula manja ake pofuna kuonetsa kuti akukhumba ndipo akupempha chinachake kuchokera kwa Ambuye. Mu kutamanda, ndi chizindikiro cha kumukweza ndi kupereka ulemu kwa Mpulumutsi wathu komanso Atate wathu wakumwamba.

Pamene nyimbo za ku Zioni zimayimbidwa, manja amakwezedwa m'mwamba pofuna kuonetsa kutamanda ndi ulemu kwa Ambuye. Chikhoza kukhala chizindikiro cha chitsimikizo kapena kuimira pemphero loonetsa kufuna komanso kukhumba kwa china chake choposa zimene zikuyimbidwa kapenanso kulankhulidwa.



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

Kalozera posanthula Baibulo

Mutu: Matamando

Kuwerenga Malemba: Fuulirani kwa Yehova, inu, dziko lonse lapansi. Tumikirani Yehova ndi chikondwerero: Idzani pamaso pake ndi kumuimbira mokondwera. ... Lowani kuzipata zake ndi chiyamiko, ndi kumabwalo ake ndi chilemekezo. —Masalmo 100:1-2, 4

Tanthauzo: Kupereka matamando ndi chinthu chimene chimachitika poonetsa kuvomereza, kuyamikira, kapena kuchitira umboni. Ndiko kulambira kudzera mu mau kapena nyimbo zimene zimalemekeza ndi kumukweza Ambuye.

Chidule: Mulungu akuyenera matamando ndi malemekezo. Si udindo chabe koma ndi cholowa cha anthu ake kuti amukweze Iye nthawi zonse mu mau ndi mu nyimbo. Matamando enieni si a ku thupi ayi koma amayenderera kuchokera mkati mu mzimu komanso mu moyo umene uli wodzaza ndi chiyero. Muli mphamvu mu kutamanda ndipo kumatsekula makomo ofikira pamaso pa Mulungu ndi kulandira madalitso ake.

I. Matamando akulamulidwa

- A. Chivumbulutso 19:4-7 Kwa atumiki ake onse.
- B. Aroma 15:9-11 Kuitanidwa kuti tikondwere ndi kulemekeza.
- C. Masalmo 117:1-2 Anthu onse ndi maiko onse.
- D. 1 Mbiri 16:23-36 Wamkulu woyenera kutamandidwa.
- E. Ahebri 13:15 Nsembe ya matamando.

II. Imbani ndipo yamikani

- A. Masalmo 9:11 Imbani zolemekeza.
- B. Masalmo 107:1-2 Oomboledwawo atero.
- C. Aefeso 5:19-20 Imbani ndipo yamikani.

III. Zifukwa zolemekezera

- A. Luka 10:19-20 Maina athu alembedwa Kumwamba.
- B. 1 Samuele 4:5-6 Kupezeka kwa Mulungu.
- C. Masalmo 29:2 Ulemerero woyenera dzina lake.
- D. Yoweli 2:26 Chifukwa cha zimene Mulungu watipatsa.
- E. Masalmo 147:1 Kwabwino ndi koyenera.

IV. Liti komanso kuti

- A. Afilipi 4:4 Sangalalani nthawi zonse.
- B. Masalmo 35:28 Tsiku lonse.
- C. 1 Petro 4:12-13 Mu mayesero, masautso ndi mazunzo. (Luka 6:22-23).
- D. Masalmo 149:1 Mu mabwalo a oyera mtima.
- E. Masalmo 150:1-2 Pa dziko lonse lapansi.

V. Zitsanzo za Kulemekeza

- A. Luka 18:42-43 Munthu osaona achiritsidwa.
- B. Machitidwe 3:8-9 Munthu wolumala achiritsidwa.
- C. Luka 19:35-40 Ophunzira akondwera.
- D. Luka 23:44-49 Kenturiyo waChiroma.

VI. Kulemekeza kwa Zioni

- A. Yesaya 60:18 Zipata zikutchedwa Malemekezo.
- B. Masalmo 137:1-4 Ukapolo umatchinga kutamanda.
- C. Yesaya 35:8-10 Njira yaikulu ya chiyero.
- D. Yesaya 61:3 Chovala cha matamando.
- E. 1 Petro 2:9 Onetsani matamando.
- F. Yesaya 12:3-6 Fuulani ndipo kwezani mau.

VII. M'mene mumatandire ndi kulambira

- A. Yohane 4:21-24 Mu mzimu ndi m'choonadi.
- B. 1 Atesalonika 5:16-19 Musazime.
- C. Ahebri 12:28 Moopa ndi kupereka ulemu wa umulungu.
- D. 1 Petro 4:10-11 Yesu akuyenera kutamandidwa.
- E. Yoweli 2:26-27 Tamandani ndipo musachite manyazi.
- F. 1 Akorinto 14:40 Mwadongosolo ndiponso moyenera.

VIII. Kulemekeza kooni ndi kulemekeza kwabodza

- A. Yesaya 29:13 Mtima uli kutali ndi Mulungu.
- B. Yesaya 42:8-10 Ulemerero wa Mulungu superekedwa kwa wina aliyense.
- C. Masalmo 138:1 Ndi mtima wonse.
- D. Afilipi 3:3 Osati mwa thupi.

IX. Mphamvu ya Kutamanda

- A. 2 Mbiri 20:20-22 Yehosafati.
- B. Yoswa 6:16 Nkhondo ya Yeriko.
- C. Machitidwe 16:25 Paulo ndi Sila.

Kumaliza

*Zonse zakupuma zilemekeze Yehova.
Aleluya. —Masalmo 150:6*





O Lemekezani Yehova

Kupereka matamando kwenikeni kwa Mulungu ndiko kulambira kwa uzimu ndi kuthupi. Kutamanda Mulungu sikutanthauza kungobwereza mau kapena m'mene munthu akumvera m'thupi, komanso ndi chinthu chochitika pofuna kumvera Ambuye pamene Mulungu akuthokozedwa, kulemekezedwa ndiponso kukwezedwa.

“Ngati mumtima muli matamando ndi mayamiko, zidzitulukira pakamwa ngati chopereka kwa Ambuye.”

Kutamanda kukulamulidwa

Kutamanda si ganizo chabe koma ndi lamulo loperekedwa mu Baibulo kokwana ka 250. Mfumu Davide anali munthu amene amadziwika ndi kutamanda ndipo anaphunzira chinsinsi chakufika pamaso pa Mulungu. “Lowani mu zipata zake ndi chiyamiko, ndi mabwalo ake ndi chilemekezo, Myamikeni, lilemekezani dzina lake” (Masalmo 100:4). Langizo lakuti “Tumikirani Yehova ndi chikondwerero” ndiponso “Idzani pamaso pake ndi kumuimbira mokondwera” (Masalmo 100:2) ali oposa machitidwe a mu Chipangano Chakale. Mulungu amalemezedwa ndi kukwezedwa pamene timtamanda ndiponso kumulemekeza, kutamanda kotero ndiye udindo wa anthu. Anthu ambiri ojera mtima amaona kutamanda ngati chisankho kapena chinthu chakuti akhoza kuchita ngati atafuna malingana ndi m'mene munthuyo aliri. Pa Chivumbulutso 19:5, 7 akuti “Ndipo mau anachokera ku mpando wachifumu ndi kunena Lemekezani Mulungu wathu akapolo ake onse....Tikondwerere, tisekerere, ndipo tipatse ulemerero kwa Iye.” Aroma 15:10-11 akupitiriza kutsindika lamulo ili lakuti anthu ONSE akuyenera kutamanda Ambuye ndi kumukweza.

Mulungu ali woyenera matamando

“Lemekezani Yehova, amitundu onse; muimbireni, anthu onse. Pakuti chifundo chake cha pa ife ndi chachikulu; ndi choonadi cha Yehova nchosatha. Haleluya” (Masalmo 117:1-2). 1 Mbiri 16:23-36 ikulongosola mokoma ndithu za ukulu ndi kuyenera kwa Yehova amene tikuyenera kumtamanda. Iye ndi mlengi wa dziko lonse ndipo ali ndi mphamvu zonse, ulemu wonse komanso ulemerero wonse. Iye ndi wabwino ndipo chifundo chake nchosatha ku nthawi zonse. Iye ali Mulungu wa chipulumutso chathu. Pa ndime 29 akutilangiza kuti: “Mchitireni Yehova ulemerero wa dzina lake; bwerani nacho chopereka, ndipo fikani pamaso pake; lambirani Yehova m'chiyero chokometsetsa.”

Nsembe ya matamando

Anthu amaonetsera kukondwa kapena chisoni chawo mosiyanasiyana, koma matamando ndiyo nsembe imene Mulungu amayembekezera kuti ichitike mu nyengo ino ya chisomo. “Potero mwa Iye tipereke chiperekere nsembe yakuyamika Mulungu, ndiyo chipatso cha milomo yovomereza dzina lake” (Ahebri 13:15). Ngati mumtima muli matamando ndi mayamiko, zidzitulukira pakamwa ngati chopereka kwa Ambuye. Kukhoza kukhala kovuta kutamanda ndi mau, koma kukhala moyo wokondweretsa Mulungu si chinthu chophweka konse. Kutamanda polankhula kukuyenera kuchokera mu mtima, ndipo kumabweretsa dalitso lodabwitsa.

Matamando a pakamwa

Gawo la kutamanda ndiko kumukweza Mulungu ndi mau athu “Yamikani Yehova! Haleluya! Ulemerero kwa Mulungu!” “Yamikani Yehova.... Atere oomboledwa a Yehova” (Masalmo 107:1-2). Kutamanda kukhoza kuchitikanso poyimba nyimbo. “Yimbirani zoyamika Yehova” (Masalmo 9:11). Pa Aefeso 5:19-20 akulangiza anthu a Mulungu kuti ayimbe ndi kupereka mayamiko nthawi zonse kwa Mulungu chifukwa cha zinthu zonse.

Zifukwa zotamandira Mulungu

Pali zifukwa zambiri zotamandira Ambuye. Matamando asamatengere m'mene zinthu ziliri, popeza Mulungu amakhallabe Mulungu ngakhale m'nyengo zosautsa za moyo, ndipo Iye akuyenera matamando athu. Yesu anawauza ophunzira kuti akondwere popeza kuti “maina anu alembedwa m'Mwamba” (Luka 10:19-20). Tamandani Ambuye chifukwa cha kupatsa kwake ndi chisamaliro chake (Yoweli 2:26). “Aisraele onse anafuula ndi mau okweza, kotero kuti dziko linachita chivomezi” (1 Samueli 4:5-6) pamene likasa lachipangano la Yehova linafika ku zithando zawo. Choncho, zidzikhalanso chimodzimidzi ndi ife lero pamene kuppezeka kwa Ambuye kuti pakati pa anthu ake. Padzikhala kukondwera ndi kutamanda. Chimakhala chinthu

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

chonyaditsa pamene tili ndi overa mtima, ndipo pamodzi tonse tikulemekeza Mulungu mu mau ndi mu nyimbo motsogozedwa ndi kudzoza kwa Mzimu Woyera. “Pakuti kuimbira zomlemekeza Mulungu wathu nkokoma; pakuti chikondwetsa ichi, chilemekezo chiyenera” (Masalmo 147:1). Kusowa kwa matamando pafupipafupi pakati pa overa mtima chidzikhala chizindikiro chakuti zinthu sizili bwino, popeza Mulungu anakhala m'matamando.



“Matamando si chinthu chongochitika pa nthawi ya chipembedzo basi, koma chidzikhala gawo limodzi la moyo wathu wa tsiku ndi tsiku.”

Zitsanzo za mu Baibulo

Pali machitidwe komanso zitsanzo za kutamanda mu mpingo woyamba. Pamene Yesu anachiritsa munthu wosaona, munthuyo analemekeza Mulungu ndi anthuwo “ndi kulemekeza Mulungu: ndipo anthu onse pakuona, anachitira Mulungu mayamiko” (Luka 18:42-43). Pamene munthu wopuwala miyendo anachiritsidwa pa chipata cholowera mu Kachisi, iye anapita akulumphana ndi kutamanda (Machitidwe 3:8-9). Iye anali wokondwa chifukwa cha zimene Mulungu anamuchitira, sanangoyenda ayi koma analumphana ndi chimwemwe. Imodzi mwa nkhani zochititsa chidwi yokhudza matamando ndiyo pamene Yesu anabwera akukwera pa mwana wa bulu pamene amalowa mu Yerusalemu ndipo “unyinjira wonse wa ophunzira anayamba kukondwera ndi kuyamika Mulungu ndi mau aakulu, chifukwa cha ntchito zonse zamphamvu anazona” (Luka 19:37). Sikuti anali

Titamande nthawi zanj

Anthu a Mulungu akuyenera kukondwera nthawi zonse (Afilipi 4:4) ndipo adzikhala okonzeka kupereka matamando kwa Ambuye kwa tsiku lonse lathunthu (Masalmo 35:28). Kukondwera si kwa nthawi zabwino zokha komanso ngakhale mu nthawi za mayesero ovuta, mazunzo komanso masautso (1 Petro 4:12-13). Mukhoza kudabwitsika m'mene zinthu zingasinthire ndiponso mzimu umene ukhoza kubwera m'nthawi zovuta pamene ulemerero ndi matamando ziperekedwa kwa Mulungu. Matamando si chinthu chongochitika pa nthawi ya chipembedzo basi, koma chidzikhala gawo limodzi la moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Mulungu akuyenera kulemekezeka mu msonkhano (Masalmo 149:1) ndiponso mu malo overa a chilengedwe chake (Masalmo 150:1-2). Matamando enieni ndi chiwonetsero cha chikondi komanso kupembedza Ambuye kuchokera mu mtima wangwiro.

Petro yekha kapena ophunzira ake amene anamutanda ndi mau ofuula—koma anthu onse anakondwera. Afarisi anawadzudzula anthuwo koma Yesu anawayankha mu ndime 40 nati: “Ndinena ndi inu, ngati awa akhala chete miyala idzafuula.” Kodi ndani amene adzatamanda Ambuye ngati anthu a Mulungu satero? Kodi anthu a Mulungu akhale mwamantha poopa kuti anenedwa kuti akulakwitsa? Kodi ndi miyala imene ikufuula?

Zioni apereka matamando

Makoma a Zioni (Mpingo wa Mulungu) ndiwo chipulumutso ndipo zipata za Zioni ndizo matamando (Yesaya 60:18). Pamene anthu adutsa pa zipata za matamando, iwo amakwezeka pamwamba pa mavuto a moyo uno ndipo amakwera kukafika kumene kuli ulemerero wodabwitsa wa Yesu Khristu. Iwo amasanduka gawo limodzi la ulemerero weniweni wa Mulungu. Mdaniyo amafuna kuzimitsa matamando a anthu a Mulungu. Pamene anali ku ukapolo wa ku Babiloni, ana a Israele anapachika azeze awo pa mitengo, nalira, ndipo sanayimbenso nyimbo za Zioni (Masalmo 137:1-4). Komabe, pamene iwo anabwerera ku Zioni pa msewu waukulu wa chiyero, iwo anabwera ndi nyimbo komanso chimwemwe chamuyaya. Zimenezi ndi zomwe anthu a Mulungu akuyenera kumachita. Overa mtima “kuti mukalalikire zoposazo za Iye amene anakuitanani mutuluke mumdimba, mulowe kuunika kwake kodabwitsa” (1 Petro 2:9).

Matamando otsogozedwa ndi Mzimu

Yesu anaphunzitsa nati “olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi m'choonadi” (Yohane 4:23). Kutamanda kovomerezeka ndiko kotsogozedwa ndi Mzimu komanso kumene kuvomerezeka ndi moyo wa choonadi. Kutamanda kuchokere mkati mwathu, “Musazime Mzimuyo” (1 Atesalonika 5:19) koma matamando a Mulungu awonekere. Kutamanda mu chipembedzo pamene mulipo gulu si chionetsero cha kuchita zinthu zokanika kudzigwira, popeza kulambira kumayenera kuchitika mowopa ndi kulemekeza Mulungu (Ahebri 12:28). Zinthu zonse zichitike “koyenera ndi kolongosoka” (1 Akorinto 14:40), komatu pakhale ufulu wa kutamanda ndipo munthu asachite manyazi (Yoweli 2:26-27). Khristu ndiye amene tikuyenera kumulemekeza (1 Petro 4:10-11), ndipo matamando asakhale chinthu chongosangalatsa kapena kufuna kuonetsera ntchito ya thupi (Afilipi 3:3).

Mphamvu mu matamando ovomerezeka

Ambiri amalambira Mulungu ndi milomo yawo pamene mitima yawo ili kutali ndi Iye (Yesaya 29:13). Mulungu amakana matamando a mtundu wotere popeza Iye amafuna anthu kuti amutamande ndi kumukonda Iye ndi mtima wao onse. Chifukwa chakuti anthu ambiri mu misonkhano ya Chikhristu amanyozetsa mau a “kutamanda ndi kulambira,” ifeyo tisalolere kuti mdaniyo alande kapena abe chimene chili cha anthu ake a Mulungu. Pali mphamvu yaikulu mu kutamanda kwa munthu payekha komanso kwagulu pamene anthu ake amamulemekeza ndi miyoyo yawo, mitima yawo, komanso milomo yawo. ■

Funso Yankho

Kodi kumakhala ngati kusutsana pamene munthu akunena za matamando kuchokera m' buku la Masalmo komabe osagwiritsa ntchito zida zoyimbira panthawi ya chipembedzo?

Mfumu Davide, ngakhale kuti anachita zoipa zambiri, anali munthu wokonda kulambira ndi kutamanda Mulungu. Masalmo ali wodzaza ndi mau a matamando a kwa Mulungu. Kawirikawiri iye amalimbikitsa ena kuti atamande osati mu nyimbo mokha komanso ngakhale mu zida zoyimbira ngakhale kuvina monga ziliri pa Masalmo 150. Davide anali pansi pa lamulo la Mose osati pansi pa choonadi cha Yesu Khristu. Pali machitidwe ndi zikhalidwe zina za Davide zimene zili zoyamikirika komanso zothandiza ngakhale pano pamene tili mu nyengo ya chisomo.

Sikuti pali kusiyana pamene tigwiritsa ntchito zimene ananena Davide kapena aneneri akale pofuna kuphunzitsa, kudziwitsa ndiponso kulimbikitsa. Ngati pali chinachake chotsutsana ndi chiphunzitsa cha mu Chipangano Chatsopano, sititsatiranso chitsanzo chimenecho. Pamene matamando a Davide ali olimbikitsa, popeza ena a iwo amagwirizana ndi chiphunzitsa cha mu Chipangano Chatsopano, zina mwa zimene iye amachita sizinagwirizane ndi chiphunzitsa komanso machitidwe a oyera mtima a mu Chipangano Chatsopano.

Ngakhale kuti Davide anapereka nsembe, chakhumi, nalambira pogwiritsa ntchito zida zoyimbira, mpingo woyamba sunachita zimenezo. Iwo analambira mu mzimu ndi m'choonadi kusiyana ndi zokhumba za thupi ndiponso miyambo ya malamulo. Palibe chiphunzitsa mu mpingo wa mu Chipangano Chatsopano chimene chimalimbikitsa kugwiritsa ntchito kwa zida zoyimbira, ndipo kupitirira pamene, mbiri imationetsa kuti mpingo woyamba unaphunzitsa mosutsana ndi kugwiritsa ntchito zidazo mu muzipembedzo zawo monga momwe anachitiranso akuluakulu amene anagwira ntchito yokonzanso mpingo.

Kuti mudziwe zambiri zokhudzana ndi kugwiritsa ntchito zida zoyimbira mu chipembedzo, onani Kalata ya No 21 pa: www.thegospeltruth.org

Kodi "kutamanda ndi kulambira" kwa masiku ano ndi njira yovomerezeka yolambira Ambuye?

Pali nkhani zingapo zimene zili mu funso limeneli ndipo mwina sindizikamba zonse, koma ndigawana nanu zinthu zochepe chabe zakuti mulingalire zokhudzana ndi machitidwe a masiku ano a kutamanda ndi kulambira. Choyamba ndicho chakuti kutamanda ndi kulambira pazokha ndi zinthu zimene Ambuye analamulira. Ngakhale zili choncho, kutamanda ndi kulambira kwenikweni kudzikhalala kotsogozedwa ndi Mzimu, osati kwathupi. Mipingo yambiri imakhala ndi zochitika za mayimbidwe ndi zina zokhudza nyimbo zimene zimatakasa thupi koma zili zosapindulitsa ku uzimu ndipo sizithandize moyo konse. Ngati anthu akhoza kudziyamikira mu zinthu zathupi chifukwa cha magetsi osiyanasiyana amene akuthwanima, bandi yoyimba mwaluso, ngakhale kuvina pamene nyimbo zotamanda Mulungu zikuyimbidwa, koma akachoka pamene nkukapitiriza moyo wa wauchimo, nzokaikitsa ngati zochitika zoterezo zili zovomerezeka. Zimenezi ndi zotheke ndithu komanso zoona zake nzakuti kutamanda ndi kulambira kwambiri kwa masiku ano kuti ngati kuvala chigoba chachikhristu pofuna kuphimba moyo wachidetso ndi wopanda chihero.



Mwini wake wa kulambira koona ndi Khristu. Zambiri zimene zikuchitika mu kutamanda ndi kulambira masiku ano zimakweza ndi kulemekeza mphatso za anthu komanso kuthekera kwa umunthu. Pali chinachake chimene chimatakasa ndi kupangitsa anthu kuti amve bwino chimene chikhoza kuchitika pamene munthu ali mu chipembedzo chotero, koma ndikulakalaka kuti ndione chihero ngati zotsatira za pamapeto ake. Kuyimba pakokha si kulambira, ndipo ngati kutamanda ndi kulambira kuti choncho, malingana ndi mau a wolemba wina, ndiye kuti chili ngati chinthu, "chongochitika pa kanthawi," ndipo zikatero si kulambira koona.

Kulambira kovomerezeka ndi uko kumene kumachokera mu mtima wa chikondi cha pa Mulungu, ndipo ndi mtima wa chikondi umene umaonekera pakumvera Mulungu. Ngakhale mu nthawi ya Khristu, panali iwo amene anasendera pafupi ndi Yesu ndipo ndi milomo yawo anamulemekeza koma mitima yawo inali kutali ndi Iye (Mateyu 15:8).

Zinthu zambiri zochitika masiku ano zokhudza kutamanda ndi kulambira zili zakudziko komanso zosutsana ndi zimene zili kulambira kwa umulungu. Pamene aliyense ali ndi ufulu komanso mwai wakuti akhoza kutamanda, ana a Mulungu sakuyenera kupezeka kuti akulakwitsa povomereza kapena kulekera zochitika zimene zili zosavomerezeka pamaso pa Ambuye. Tsoka ilo, kutamanda ndi kulambira kwa masiku ano sikuwasendeza anthu chifukwa mu chiyanjano chawo ndi Ambuye.

"Kulambira kovomerezeka ndi uko kumene kumachokera mu mtima wa chikondi cha pa Mulungu, ndipo ndi mtima wa chikondi umene umaonekera pakumvera Mulungu."



KODI MUKUDZIWA?

Paulo, pa 1 Timoteo 2:9, asanapereke langizo lakuti azimai adzivala modzilemekeza ndi amakhalidwe abwino, (izi ndi zimene anthu ambiri otsatira chiyero amagwirizana nazo), iye anati kwa abambo: “Chifukwa chake ndifuna kuti amunawo apemphere pamalo ponse, ndi kukweza manja oyera, opanda mkwiyo ndi makani.”



Mau a Nyengo Yake

CHOVALA CHA MATAMANDO

Yehova wapereka mafuta akukondwa m'malo mwa maliro, chovala cha matamando m'malo mwa mzimu wopsinjika. — Yesaya 61:3

Yesu Khristu anafika kudzabweretsa nkhani yabwino ku dziko losauka ndi uchimo. Iye anabweretsa machiritso auzimu ndi mamasulidwe ku mizimu imene inamangidwa kuti ipite ku gehena. Pamene panali kulira ndi chisoni, tsopano pali chimwemwe ndi mtendere. Pamene panali mzimu wotopa ndi wopsinjika, Yesu anabweretsa chovala cha matamando.

Ndi chisankho chimene anthu amapanga kuti akhalebe ndi mzimu wopsinjika mu uchimo kapena atsekule mtima wao wolemedwa ndi kulola kuti Yesu awapatse mpumulo ndi mtendere. Yehova amafunitsitsa kuwakuta ana ake mu chovala cha matamando chimene chidzabweretsa ulemerero ndi ulemu kwa Atate.

Nkofunika kukumbukira kuti chipulumutso sichitiwombola kuchokera ku zowawa zonse ndiponso kuwawidwa mtima chifukwa cha uchimo umene pakati pathu m'dzikoli. Anthu opulumutsidwa akhoza kukhala ndi mavuto a kuthupi, m'maganizo komanso ena a kanthawi kochepe. Mkati mwa mavuto amenewo, mdaniyo amafuna kumiza ana a Mulungu ndi mzimu wa kukhumudwa pamene chiyembekezo chonse chimataika ndipo mdima umabwera ndi kukhazikika. Yesu anabwera kudzatonthoza iwo akulira ndiponso kuwatumikira iwo amene akusautsika.

Pamene mzimu wa kutopa ufika kuti ukhazikike pa mapewa anu, yang'anani kwa Ambuye ndipo ndi chovala cha matamando onani manja ake otambasula. Mu mdima wandiweyani pakatikati pa usiku, mzimu wa kutopa ukhoza kugonjetsedwa ndi mzimu wa matamando. Pamene zinthu zokuzungulirani zikusokonekera, mukhozabe kutamanda Ambuye chifukwa cha chipulumutso ndi chikondi chake. Pamene mumutamanda, mitambo ya kukhala kakasi imayenera kukakatuka.

Sinthawi zonse pamene matamando amachotsa misozi, komatu ngakhale misozi imene moyowu umabweretsa ku mitima yathu ikhoza kuchotsedwa pamene tikutamanda chifukwa cha kupezeka kwa Yesu Khristu. Pamene mukuona ngati simukufuna kutamanda ndi kuyamika, pamene pangani chisankho chakutamanda ngakhale muli m'namondwe. Sinthanitsani mzimu wopsinjika ndi chovala chopambana ndiponso chowombola cha matamando. ■



Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE